# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

### ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA, LA 2025-2026 M'BOMA LA SALIMA


## DZINJA LA 2025/2026 MWACHIDULE

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/2026.

Boma la Salima likuyembekezeka kulandira mvula mlingo wokhazikika kapena kuposera apo.


Nyengo yonse ya dzinja ikuyembekezereka kuzakhala masiku apakati pa 120 ndi130

## OCTOBER 2025





M'mwezi wa October, madela ambiri a m'boma la Salima akuyembekezeka kuzakhala opanda mvula. Mvula ya **chizimalupsa** yosachepera 15mm yodza ndi mphepo komanso ziphaliwali chifukwa cha kutentha kwambiri ikuyembekezeleka kudzagwa mmadela ena.

## NOVEMBER 2025




M'mwezi wa November, madela ena m'boma la Salima a kuyembekezeka kudzalandira mvula yochepela 50 mm.


## DECEMBER 2025




Madela ambiri a azalandira mvula ya pakati pa 150–250 mm, angakhale madela ena monga TA Maganga, TA Pemba ndi TA Kuluunda adzalandira mvula yochulukirapo yokwana 250–300 mm.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kudzayamba sabata la chiwiri la mwezi wa December


## JANUARY 2026




Madela a TA Maganga, Pemba, Kuluunda ndi a m'mbali mwa nyanja atha kudzalandira mvula yokwana 300mm, pomwe madela a TA Mwaza, Kambwiri ndi Ndindi adzalandira mvula ya pakati pa 200-250mm.

Pali chiwopsezo cha ng'amba chokwana sabata lathunthu opanda mvula mu mweziwu.


## FEBRUARY 2026




Mwezi wa February ukuyembekezeka kudzalandira mvula yokhazikika kapena yochepela apo m'madera mbiri. Madela a TA Maganga, akuyembekezeka kudzalandira mvula yokhazikika kapena kuposela apo ya pafupifupi 300mm.


Sabata latunthu lopanda mvula likuyembekezeka m'mweziwu.

## MARCH 2026




M'mwezi wa March, boma la Salima likuyembekezeka kudzalandira mvula pafupifupi 150-250mm, ngakhale madela monga kwa TA Maganga ndi TA Kuluunda adzalandira mvula yochulukirapo pafupifupu 300mm.

## APRIL 2026




Mvula idzayamba kuchepa m'mwezi wa April chifukwa nyengo ya dzinja idzakhala ikupita ku mapeto. Madera ambiri mu boma la Salima adzalandira mvula yosapyola 50mm.
Dzinja likuyembekezeka kudzatha sabata la chiwiri la mwezi wa April 2026

Boma la Salima likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kuyamba kugwa sabata la chiwiri la wezi wa December 2025.


Dzinja likuyembekezeleka kuzatha sabata la chiwiri la mwezi wa April 2026.

Nyengo yonse ya dzinja ikuyembekezereka kuzakhala masiku 120 kufikira 130.

Ng'amba yokwana sabata limodzi ikuyembekezeka mu boma la Salima

## SALIMA

| SALIMA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.1 | 4.9 | 7.1 |
| NOV | 14.3 | 38.5 | 24.2 |
| DEC | 159.3 | 295.6 | 223.2 |
| JAN | 204.6 | 407.1 | 341.1 |
| FEB | 199.4 | 327.9 | 264.5 |
| MAR | 159.8 | 271.6 | 428.1 |
| APR | 27.3 | 62.6 | 63.9 |





**Ulosiwu udzawunikidwanso mu mwezi wa December 2025**
Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:
The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email:
metdept@metmalawi.gov.mw ; Website:
www.metmalawi.gov.mw



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: